



**"CHONDE,
NDIONETSENI
ULEMERERO
WANU"**

Phunziro 12
September 20, 2025



“Ndipo Iye anadutsa kutsogolo
kwa Mose akulengeza kuti,
“Yehova, Yehova, Mulungu
wachifundo ndi wokoma mtima,
wosapsa mtima msanga, wodzaza
ndi chikondi chosasinthika ndi
kukhulupirika, waonetsa chikondi
chosasinthika kwa anthu
miyandamiyanda, wokhululukira
zoyipa, kuwukira, ndiponso
tchimo, komatu salekerera
ochimwa kuti asalangidwe. Iye
amalanga ana ndi zidzukulu
chifukwa cha machimo a makolo
awo mpaka m'bado wachitatu ndi
wachinayi.”


Eksodo 34:6, 7

Palibe kukayika konse. Mulungu ndi Mose anakhala abwenzi apamtima.

Izi sizinachitike mwadzidzidzi. Zinachitika mwapang'onopang'ono. Zinayamba ali mwana, pamene amayi ake anamuwuzaza za Mulungu wodabwitsa amene ankamutumikira.

Ubwenzi wawo unalimbidsidwa muzochitika zosiyanasiyana zimene anali nazo pa Phiri la Sinai, ndipo unkakula kufikira tsiku limene Mulungu anayitana Mose kuti apume.

Machaputala 33 ndi 34 a m'buku la Eksodo analemba za nthawi yapadera mubwenzi umenewu: pempho la Mose lofuna kuona ulemmerero wa Mulungu.



Mulungu ndi Mose:



Kukumana ndi Mulungu (Eksodo 33:7-11)



Kumudziwa Bwino Mulungu (Eksodo 33:12-17)



Ulemelo wa Mulungu:



Chilakolako chofuna kudziwa ulemmerero wa Mulungu (Eksodo 33:18-23)



Masomphenya a ulemmerero wa Mulungu (Eksodo 34:1-28)




Zotsatira za kuona ulemmerero wa Mulungu (Eksodo 34:29-35)

MULUNGU
NDI MOSE

KUKOMANA NDI MULUNGU

"Mose akamalowa mu tenti, chipilala cha mtambo chimatsika ndi kukhala pa khomo pamene Yehova amayankhula ndi Mose." (Eksodo 33:9)

Mose anakumana ndi Mulungu mu chihema, pamene analankhula naye maso ndi maso (Eksodo 33:7-11).



Kufotokoza pang'ono: mawu akuti 'maso ndi maso' sanatanthauze kuti ankaonana maso ndi maso mwa kuthupi, koma kuti ankakhala ndi ankakambirana momvana bwino (Ngakhale Mose sanawone nkhope ya Mulungu konseko.

Mose anakhala mtumiki wokhulupirika wa Mulungu (Ahebri 3:5), nyale yosazimitsa mumdima, ndiponso mneneri wachitsanzo chabwino.

Ubwenzi wa pakati pa Mulungu ndi Mose unakula pang'onopang'ono



Mulungu anauzira Mose kulemba Yobu ndi Genesis



Mulungu anamuyitana iye kuchokera mu chitsamba choyaka moto



Mose anaona mmene Mulungu anagonjetsera milungu ya Aigupto



Anawona Nyanja Yofiira ikutseguka kuti Israeli amasulidwe ku ukapolo



Iye ankaona mmene Yehova ankatsogolera Aisraeli pa Phiri la Sinai



Anakhala limodzi pa phiri kwa masiku 40 athunthu



Ubwenzi wawo anapitiriza kukula tsiku ndi tsiku

KUDZIWA BWINO MULUNGU

Ngati mwakondwera nane ndiphunzitseni njira zanu kuti ndikudziweni ndi kupitiriza kupeza chisomo pamaso panu. Kumbukirani kuti mtundu uwu ndi anthu anu.” (Eksodo 33:13)

Pamene Mulungu anauza Mose kuti lye sadzapita ndi anthuwo ku Kanani (Eksodo 33:1-3), zokambirana zosangalatsa zinayambika (Eksodo 33:12-17).

Mulungu Ndiwe bwenzi langa ndipo wapeza chisomo pamaso panga

Mose Ngati ndi choncho, ndiphunzitseni njira zanu kuti ndikudziweni.

Mulungu Ine ndemwe ndidzapita pamodzi ndi iwe, ndipo ndidzakupatsa mpumulo.

Mose Ngati inu simupita nafe, musatitumize kuti tipite, kutichotsa pano.

Mose Kodi wina adzadziwa bwanji kuti inu mwandikomera mtima ngati simupita nafe?

Mulungu Chabwino, ndidzachita zimene iwe wandipempha chifukwa Ine ndikukondwera nawe, ndipo ndiwe bwenzi langa.

Mose anakhala ndi Mulungu kwa masiku 40, akulandira Malamulo Khumi ndi malangizo omangira kachisi. Tsopano iye anali kachiwiri pamaso pa Mulungu, kupembedzera anthu. Ankaoneka kuti amamudziwa bwino Mulungu chifukwa ankalankhula naye bwinobwino. (Eksodo 33:13) Kodi anafunika kumudziwa mu njira yotani? Kodi inunso mufuna mutamudziwa mu njira yotani?



ULEMELEERO WA MULUNGU

CHIKHUMBO CHA KUDZIWA ULEMERERO WA MULUNGU

"Kenaka Mose anati, "Tsopano ndionetseni ulemerero wanu."" (Eksodo 33:18)



Mose anafunsa kuti: "Ndionetseni ulemerero wanu (Eksodo 33:18)



Mulungu anayankha kuti:
"Ndidzakusonyezani ubwino wanga
(Eksodo 33:19)



Zimene Mulungu anamuonetsa
zinali khalidwe lake (Eksodo 34:6-7)



**Ulemerero
wa Mulungu
ndi ubwino
wake, ndilo
khalidwe
lake**

Ellen G. White akuwonjezera kuti ulemerero wa Mulungu uli m'kuthandiza ana ake; kulandira ochimwa amene atembenuka; ndi kupereka zonse zofunika kuti asinthe.

Choncho, "ulemerero" wathu ndi kusonyeza makhalidwe a Mulungu m'miyoyo yathu (2 Ako. 1:12; 3:18 .


Pamene tiyang'ana pa Mtanda, timakhala ndi vumbulutso lalikulu la ulemerero wa Mulungu, ubwino wake, ndi makhalidwe ake.

MASOMPHENYA A ULEMERERO WA MULUNGU

"Ndipo Iye anadutsa kutsogolo kwa Mose akulengeza kuti, "Yehova, Yehova, Mulungu wachifundo ndi wokoma mtima, wosapsa mtima msanga, wodzaza ndi chikondi chosasinthika ndi kukhulupirika," (Eksodo 34:6)

Mulungu anasonyeza ulemerero wake kwa Mose panthawi yachisanu ndi chiwiri pamene anakwera phiri la Sinai. Mose ankadzionetsera pamaso pa Mulungu kangati, ndipo ndi pa nthawi yanji komanso ndi cholinga chotani?

- 1** Kulandira maziko a pangano (Eksodo 19:3-7)
- 2** Kupereka yankho la anthu ndi kulandira malangizo okhudza kuonekera kwa Mulungu ku Sinai (Eksodo 19:8-14)
- 3** Kulandira malangizo atsopano (Eksodo 19:20-25)
- 4** Kulandira malamulo ogwirizana (Eksodo 20:21; 24:3)
- 5** Kulandira Malamulo Khumi olembedwa ndi chala cha Mulungu, ndi chitsanzo cha Malo Opatulika (Eksodo 24:12, 18; 32:15)
- 6** Kupembedzera tchimo la mwana wa ng'ombe wagolide (Eks. 32:30)
- 7** Kuti Mulungu amuonetse ulemerero wake, ndi kulandira magome atsopano okhala ndi Malamulo Khumi (Eksodo 34:1-5)



Masomphenya a ulemerero wa Mulungu anasonyeza kudziwitsa kwa Mulungu yekna za knaulowe lake (Eksodo 34:6-7). Ataona chikondi cha Mulungu m'njira imeneyi, Mose analambira (Eksodo 34:8; 1 Yohane 4:19). Potsiriza, Mulungu anatsimikiziranso pangano lake ndi Israeli ndipo anakhululukira tchimo la mwana wa ng'ombe wagolide.

ZOTSATIRA ZAKUONA ULEMERERO WA MULUNGU

“Mose anatsika kuchokera m’Phiri la Sinai pamodzi ndi miyala iwiri ija ya pangano m’manja mwake. Iye sanazindikire kuti nkhope yake imanyezimira pakuti anayankhula ndi Yehova.” (Eksodo 34:29)



Mose anali atalankhula ndi Mulungu “maso ndi maso” kangapo konse m’mbuyomo, ndipo kufikira nthawi, nkhope yake inali isanawaleko. N’chifukwa chiyani nthawi imeneyi zinasiyana? Ndipo dziwani kuti kusintha kumeneku kunapitiriza nthawi yayitali (Eksodo 34:34-35).

Tsopano Mose anamudziwa bwino Mulungu. Ubwenzi wake unali utakhwima. Anali kusinkhasinkha za ulemmerero wa Mulungu, ndipo anasandulika ndi ulemmerero umenewo.

Pofotokoza nkhani imeneyi, Paulo akutipempha kuti titsatire chitsanzo cha Mose ndi kulingalira za ulemmerero wa Mulungu kuti tisandulike monga mmene iye anakhalira (2 Akorinto 3:12-18) .

Mose ndi chitsanzo chimene chimasonyeza zimene Mulungu angatichitire tikamulola kuti asinthe makhalidwe athu n’kutiumba m’chifanizo chake.



“Mukuganiza kuti Mulungu adadzudzula Mose chifukwa cha kudzikuzwa kwake? Ayi, ndithudi. Mose sanapemphe izi mwachidwi chopanda pake. Anali ndi cholinga. Anaona kuti ndi mphamvu zake yekha sangathe kuchita ntchito ya Mulungu moyenera. Anadziwa kuti ngati angalandire masomphenya omveka bwino a ulemerero wa Mulungu, adzatha kupitiriza ntchito yake yofunika kwambiri osati ndi mphamvu zake, koma ndi mphamvu ya Yehova Mulungu Wamphamvuyonse. Moyo wake wonse unkalakalaka Mulungu; ankafuna kudziwa zambiri za Iye, kuti amve kuyandikira kwaumulungu munthawi ya mavuto kapena chisokonezo chilichonse. Sikunali kudzikonda komwe kunapangitsa Mose kupempha kuona ulemerero wa Mulungu. Cholinga chake chokhacho chinali kufuna kulemekeza Mlengi wake bwino kwambiri”